KUMVETSETSA ZA
MWANA WA MWAMUNA WA MULUNGU



Maphunziro mu
Chiphunzitso Cha Khristu
Ndi
Brian J. Kocourek

Mwana wa Mwamuna wa Mulungu

2 Yohane 8 – 9*;* ***8*** *Mudzipenyerere nokha, kuti mungataye zimene tazichita koma kuti mulandire mphoto yokwanira.* ***9*** *Yense wakupitirira, wosakhala mchiphunzitso cha Khristu alibe Mulungu; iye wakukhala mchiphunzitso, iyeyo ali nawo Atate ndi Mwana.* ***10*** *Munthu akadza kwa inu, osatenga chiphunzitso ichi, musamulandire iye kunyumba, ndipo musamulankhula.* ***11*** *Pakuti iye wakumulankhula iye ayanjana nazo tchito zake zoipa.*

Tsopano, awa ndi mawu a mphabvu ochokera kwa mtumwi Yohane, koma ofunika kwambiri kwa mmodzi kutsegula makutu awo kuti amve. Chifukwa anati ngati mulibe chiphunzitso cha Khritsu, ndiye kuti mulibe Mulungu. Ndipo motero anati chiphunzitso cha Khristu ndi Mulungu mmodzi amene anali ndi Mwana. Iye anati kuti inu mukhale ndi chiphunzitso cha Khritsu, muyenera kukhala ndi zonse Atate ndi Mwana.

#1) PALI MULUNGU MMODZI YEKHA ndipo potero pali Munthu mmodzi yekha amene ali Mulungu.

Eksodo 20:2-3 *Ine ndine Mulungu wako, Usakhale nayo milungu yina.*
Deuteronomo 6:4 *Ambuye Mulungu wathu ndi Ambuye Mmodzi.*
Yesaya 54:5 *Woyera Mmodzi wa Israel, Wosakhala awiri, osakhala atatu koma mmodzi.*
Yohane 17:3 *Mulungu mmodzi owona* **Aroma 15:6** *Mulungu, ngakhale Mulungu wako,*
1 Akorinto 8:6 *Mulungu mmodzi Atate,* **15:4** *kwa Mulungu,ngakhale Atate Wako,*
2 Akorinto 1:3 *Mulungu, ngakhale Atate Wako*
Aefeso 1:7 *Mulungu, wa Ambuye Yesu Khritsu,* **4:6** *Mulungu mmodzi ndi Atate wa onse,*
1 Atesalonika 3:13 *Mulungu, ngakhale Atate wathu,*
2 Atesalonika 2:16 *Mulungu, ngakhale Atate wathu,*
Yakobo 3:9 *Mulungu, ngakhale Atate wathu,*
2 Yohane 3:9 *kuchokera kwa Mulungu Atate,*
Yohane 8:54 *iye ndi Mulungu wanu*:

#2) MMENE YESU NDI MULUNGU ANALILI MMODZI. Monga mmene ife ndi mulungu tiyenera kukhala Mmodzi:
Yohane 10:30-38 *Ine ndi Atate wanga ndife Mmodzi, Atate wanga amakhala mwa ine….*
Yohane 14:8-10 *pamene mwaona Ine mwaona Atate wanga, Atate wanga amakhala mwa Ine,*
Yohane 17:11 *kuti akhale mmodzi, monga ife tiriri.* Ndipo tingakhale bwanji mmodzi ngakhale Yesu ndi Atate wake anali mmodzi? **Yohane 17:21** *kuti onse akhale mmodzi, monga inu, Atate, muli mwa Ine, ndi Ine mwa Inu, iwonso akhale mmodzi mwa ife*: **22** *ulemerero umene Inu munandipatsa Ine ndawapatsa iwo; kuti akhale mmodzi, monga ife tiriri mmodzi*; kotero ndikofunika kuti tikhale mmodzi polandira mawu omwewo amene amatibweretsa ku ulemerero omwewo kapena ku malingaliro omwewo monga a Atate. *Ulemerero umene mwandipatsa ine ndawapatsa iwo, kuti akhale mmodzi, monga ife tiri mmodzi.*

#3)YESU ANALI NDI MULUNGU: Mulungu ndi oyima payekha ndipo iye samayakha pa wina aliyense. Iye alibe wina aliyense pamwamba pake amene ali Mulungu. Kotero, ngati Yesu [Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] anali Mulungu, nanga chifukwa chiyani Iye amalakhula za wina amene ali Mulungu? Ndipo ngati ali ndi Mulungu ndiye Mulungu ameneyo ndi ndani ngati Iye mwini ndithu ndi Mulungu? Kotero Yesu, “Mwana wa Mulungu,” sanali “Mulungu Mwana,” koma iye anali “Mwana wa Mulungu”. Icho chikutathauza kuti iye anali ndi Mulungu ndipo Mulungu ameneyo anali Atate ake.

Yohane 20:17 *kwa Mulungu wanga, ndi Mulungu wanu,* **Chibvumbulutso 3:12 Masalimo 22:1 Mariko 15:34 Mateyu 27:46** *Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwandisiyiranji ine*? Tsopano, liu ili mwandisiyiranji litathauza kusiyidwa kwathuthu. Nanga Yesu analira bwanji kwakukulu kuti Mulungu anamusiya iye ngati mwamuna Yesu anali Mulungu? Kodi Mulungu angadzisiye yekha kwathuthu kuchokera kwa Iye Mwini?

 # 4) YESU SANADZINENEREPO KUKHALA MULUNGU, IYE ANALI MWANA WA MWAMUNA WA MULUNGU.

Yohane 10:36 *Ine ndine Mwana wa Mwamuna wa Mulungu?*
Yohane 8:54 *atate wanga amene inu mumati, kuti Iye ndi Mulungu wanu*:
Aefeso 1:3,17 *Mulungu ndi Atate wa Ambuye Yesu Khristu,* **1 Petulo 1:3 Aheberi 1:8,9 Masalimo 45:6,7 Chibvumbulutso 1:6, Mateyu 16:16** *mwana wa Mulungu wa moyo.*
1 Petulo 1:3 *wodala akhale Mulungu ndi Atate wa Ambuye Yesu Khristu,*
2 Petulo 1:17 *Mulungu Atate…. Uyu ndi mwana wanga wokondedwa, mwa iyeyu ine…*
2 Akorinto 1:3,11:31 *Mulungu ndi Atate wa Ambuye Yesu Khristu,*
2 Akorinto 1:3 *wodala akhale Mulungu ngakhale Atate wa Ambuye Yesu Khristu.*
1 Akorito 8:6 *koma kwa ife pali koma Mulungu mmodzi Atate,*
Aroma 15:6 *Mulungu, ngakhale Atate wa Ambuye Yesu Khristu.*
2 Yohane 1:3 *Mulungu Atate, ndikuchokera kwa Ambuye Yesu Khristu, mwana wa Atate,*
2 Yohane 1:9 *iye amene ali ndi chiphunzitso cha Khristu ali ndi onse Atate ndi Mwana*

Nanga bwanji Yesu Iye mwini, ananena chiyani zokhudzana ubale Wake ndi Atate wake?

Yohane 20:17 *Atate wanga, ndi Atate wanu; ndi kwa Mulungu wanga, ndi kwa Mulungu wanu.*
Yohane 2:16 5:17,43 6:32,65, 8:19,28,38,49,54, 10:17,18,25,29,30,32,37, 12:26, 14:2,7,12,20,21,23, 15:1,8,10,24 18:11, 20:21 *Atate wanga,*

 # 5) MULUNGU NDI WAMKULU KOPOSA YESU

Yohane 10:29 *Atate wanga ndi wamkulu koposa onse* **14:28** *pakuti Atate wanga ndi wamkulu koposa Ine.* **Mateyu 20:23, 1 Akolinto 15:24-28** *obvera kwa Atate*
Zakariya 3:8 Mateyu 12:18, Afilipo 2:7,8 *ngati Kapolo*
Aroma 5:19 *obvera kwa m'modzi*

Taonani kuti Yesu anabvomereza moona kuti Atate ndi wamkulu koposa Iye mwini. Mau awa wamkulu anathandauzidwa kuchokera ku liu la chi Greek limene silikutathauza kukhala wamkulu kokha koma wachikulire. Ndipo pamene a Utatu

akuuza kuti Yesu anali wofanana kwa muyaya ndi kukhala wofanana ndi Atate, zingakhale bwanji pamene Mwana wa Mulungu akukana ichi Iye Mwini. Ana onse ali ndi chiyambi ndiye zikanakhala bwanji kuti Mwana akhale Atate wamuyaya?

Yesaya 9:6 (A) *pakuti kwa ife mwana wabadwa*, ngati kubadwa kuti ndi chiyambi kotero osakhala kwa muyaya……ngati kubadwa mwamuna wina wake iye sanakhale kum'bereka iye. Kubadwa kuyerekeza m'ndandanda ndi mbadyo, kuyerekezatso ku bweretsa.
(B) *kwa ife mwana wa mwamuna wapatsidwa*: Iyeyu ndi mphatso, wopereka ndi wamkulu koposa mphatso.**Yohane 3:16**
(C) *ndipo boma lizakhala pa phewa lake*: **Luka 1:32** *wotchedwa mwana wamwamuna wamkulukulu: Ambuye Mulungu adzapatsa iye mpando wa chifumu wa Atate Wake Davide:*
(D) ***<u>dzina</u> lake*** *lizatchedwa Wodabwitsa, Wauphungu, Mulungu wamphavu zonse, Atate wosatha, Kalonga wa mtendere.* Tsopano, tiyeni tifufuze gawo lomaliza limene likukhuza dzina la mwana uyu,mwana uyu amene adzabadwe: *Wodabwitsa (* kodi wodabwitsa ndi dzina? Ayi) *Wauphungu* (kodi Wauphungu ndi dzina? Ayi, ndi udindo) *Mulungu waphabvu zonse*, (kodi Mulungu wamphabvu zonse ndi nzina?) *Atate wosatha*, (Atate ndi dzina? Ayi,) *Kalonga wa mtendere* (kodi Kalonga wa mtendere ndi dzina? Ayi.) Tsopano, pali dzina limodzi lokha la Atate wosatha, Mulungu wa mphabvu zonse, Wauphungu, ndi zina zotero. Ndipo dzina limenero ndi Yesu. Nanga ndipo zitathauza chiyani dzina lake **'<u>lidatchedwa</u>'** liu ili **' lidzatchedwa'** linatathauziridwa kuchokera ku liu la chi Heberi **gara** limene litathauza kulengeza . Tsono tikuona dzina lake lidzalengeza Mulungu Wamphabvu zonse,dzina lake lidzalengeza Atate wosatha, pakuti ilo ndi dzina la Atate. Yesu anatiuza icho mu,

<u>#6) YESU ANABWERA MU DZINA LA ATATE WAKE</u>

Yohane 5:43, 10:25 *Ndaza Ine mdzina la Atate wanga,*
Kotero dzina la Atate linali Yesu, dzina lomwelo linapatsidwa kwa Mwana. Mtumwi Paulo anati, *Mulungu anali **MWA** Khristu kuyanjanitsa dziko kwa iye yekha*. Iye **sadanene** kuti **Mulungu ndi Khristu**, *koma anali <u>mw</u>a Khristu.*
2 Akorinto 5:19 Mulungu anali mwa Khristu, Paulo sakuphunzitsa pano kuti Yesu anali Chidzalo cha Umulungu, koma iye akuphunzitsa kuti **MWA** Iye munakhala chidzalo chonse cha Umulungu. **Akolose 2:9** *potero **<u>mwa</u** iye munakhala chidzalo chonse cha Umulungu mthupi.*

Petulo sanaphunzitsa kuti Mzimu Woyera anali Yesu, koma anachitira umboni kuti Mulungu Atate analakhula ndipo anati Iye anatsika pansi ndi kukhala **MWA** mwana Wake wa Mwamuna. **2 Petulo 1:*17*** *iye analandira kuchokera kwa Mulungu*

Atate Ulemu ndi ulemerero,… uyu ndi mwana wanga wokondedwa, MWA iye ndikondwera. **Yohane 10:25** *ntchito zimene ndimachita mudzina la atate wanga, zimachitira umboni wa ine.*

#7) YESU ANAPEMPHERA KWA ATATE AKE AMENE ALI MULUNGU
Yohane 14:16, 16:26, 17:9,15,20 *ine ndipemphera*
Mateyu 6:9, 11:25, 14:23, 26:36,39,42,53,
Luka 6:12, 9:28, 11:2 Mariko 6:46, Aheberi 5:7,8

#8) MWANA WA MULUNGU AMATHA KUPHUNZIRA.
Chimene chikutathauza kuti **Iye sanali odziwiratu** monga Mulungu anali odziwiratu amadziwa zinthu zonse. **Aheberi 5:8** *ngakhale anali mwana, koma* ***anaphunzira kumvera*** **Luka 2:52** *ndipo Yesu* ***anachuluka*** *mu nzeru ndi mmachitidwe,* [kukhwima] *ndi mukukondedwa* [chidziwitso ndi zomchitikira] *kwa Mulungu ndi mwamuna*.

 # 9) YESU ANALI WOMVERA. Mulungu sangakhale womvera kwa wina kunja kwa iye mwini, kapena akanasonyeza wina wamkulu kuposa iye. **Aheberi 5:8** *ngakhale anali mwana,* komatu ***anaphunzira kumvera***.

#10) YESU ANAPANGIDWA WANGWIRO. Ichi chikutathauza kuti Mwana wa Mwamuna Wa Mulungu akanatha kusitha chikhalidwe chake, nzeru ndi kukula. **Aheberi 5:9** ***kupangidwa wangwiro***, ngati anapangidwa wangwiro ndiye sanabadwe njira imeneyo. Mulungu sasintha (**Malaki 3:6** ndi **Aheberi 13:8). Luka 2:40** *mwana anakula, ndipo* ***analimbika*** *wamphabvu mu mzimu,* ***kudzadzidwa ndi mzeru***: ndipo Chisomo cha Mulungu chinali pa iye. **52** *ndipo Yesu* ***anachuluka*** *mu nzeru ndi mmachitidwe,* [kukhwima] *ndi mu kukondedwa* [chidziwitso ndi zomchitikira] kwa Mulungu ndi Mwamuna.

#11) YESU ANALI WOSADZIWA, MULUNGU NDI WODZIWA.
Yesaya 40:13,14 Yesu analandira chidziwitso kuchokera kwa Mulungu **Yohane 8:28, Mariko 13:32 Mateyu 24:36** *Yesu anati, koma za tsiku ndi ola palibe mwamuna adziwa,… koma atate wanga wokha,* **Luka 2:52**, **Yohane 5:19,8:28, Mariko 13:32.**

#12) YESU SANALI WOYIMA PAYEKHA , MULUNGU NDI WOYIMA PAYEKHA.
Yesu sanatha kuchita china chili chonse pokha pokha Atate amuonetse poyamba **Yohane 5:19,30 8:28, 14:10** *Mwana sangachite china chiri chonse payekha, koma chimene awona Atate akuchita: pakuti china chiri chonse chimene achita, Iyenso mwana achita chimodzimodzi.*

#13) MWANA WA MULUNGU AMAMVERA KWA MULUNGU MU ZINTHU ZONSE.

Akorinto 15:28 *mwananso pa iye yekha amamvera kwa iye amene ayika zinthu zonse pansi pake, kuti Mulungu akhale zonse mu zonse.* **Yohane 5:19,30** *mwana wa mwamuna sangathe kuchita kanthu payekha.*

#14) YESU AMADALIRA PA ATATE KUBWEZERA ULEMERERO WAKE KWA IYE.

Yohane 17:5 *Atate inu, lemekezani ine ndi inu nokha ndi ulemerero umene Ndinali nao ndi inu dziko lapansi lisanakhadzikike.* Ichi chikutiuza kuti anali nawo koma anachokapo, ndipo tsopano akufunsa iwo ubwezeretsedwenso kwa Iye. Chodziwika kwambiri ndi mfundo yoti Iye anadzichotsera yekha mwayi wonse pamene anabwera ku dziko kudzatenga khalidwe la mwamuna, ndi kudzikhutula Iye Yekha kwathuthu ndi kutenga khalidwe la Kapolo-womangidwa.

Kuthandauza kwa Weymouth anati "***ngakhale kuyambira pa chiyambi iye anali ndi khalidwe la Mulungu, iye sanawerengera kufanana ndi Mulungu chuma cholandidwa mwamphabvu.*** *Ayi,****Iye anadzichotsa Mwini yekha ulemerero wake ndi kutenga pa Iye chikhalidwe cha mtumikiwomangidwa, mwamuna monga amuna ena onse.***

Ndipo ngati Kapolo womangidwa, maonekedwe aakulu owonetsedwa ndi kudzipereka ku chifuniro cha mwini Kapolo.

#15) YESU AMADALIRA PA CHIFUNIRO CHA MULUNGU ATATE WAKE

Aheberi 10:7,9 ,11 *ine ndinabwera kudzachita chifuniro chanu, o Mulungu* **Luka 11:2,22,42, Mateyu 6:10,26:42 7:21 12:50, Yohane 5:30, 6:38, 8:29.**

#16) MULUNGU NDI YESU SALI MMODZI MONGA MMENE CHALA CHANU CHIRI CHIMODZI, IWO ANTHU OSIYANA. **Yohane 5:32-37** awiri ayenera kuchitira umboni, wina achitira umboni wa ine. **8:17-18** ine ndi atate wanga.

#17) YESU AMADARIRA PA ATATE PA CHIPHUNZITSO CHAKE.

Yohane 7:16 *chiphunzitso changa sichanga, koma cha iye ananditumа ine.*
Yohane 5:37 *Atate iye mwini, amene ananditumа ine andichitira umboni wa ine.*

#18) ATATE ANATUMIZA MWANA.

1 Yohane 4:1 11 *Atate anatumiza Mwana wa Mwamuna kudzakhala Mpulumutsi wa dziko.*

Yohane 5:36 *koma ndiri ndi umboni waukulu ngati* [*uja] wa yohane: pakuti ntchito zimene atate andipatsa ine kuzimaliza, ntchito zomwezo zimene ndichita, zimandichitira umboni ine, kuti Atate ananditumа ine.*

#19) MULUNGU ANADZUTSA YESU KUCHOKERA KWA AKUFA.
Machitidwe 2:24,32 *Yesu uyu amene Mulungu anamuukitsa, amene ife tonse ndife mboni.*
Machitidwe 3:15,26 *Mulungu anamuukitsa mwana wake wa* mwamuna Yesu **4:10** *Mulungu anamuukitsa kwa kufa,* **Machitidwe 5:30** *Mulungu wa Atate wathu anamuukitsa Yesu,* **10:40** *Iye Mulungu anamuukitsa* **13:23,30,33,34,37 17:31** *koma Mulungu anamuukitsa Iye kwa kufa*: **Aefeso 1:20, 2:6 Aroma 4:24, 6:4 8:11 10:9** *Mulungu anamuukitsa iye kwa kufa* **Agalatiya 1:1** *Mulungu Atate, amene anamuukitsa Iye kwa kufa* ;] **2 Akorinto 4:14** *Iye amene anamuukitsa Ambuye Yesu kuchokera kwa akufa*
Akolose 2:12 *Mulungu amene anamuukitsa Iye kuchokera kwa kufa*
1 Petulo 1:21 Mulungu anamuukitsa Iye
1 Atesalonika 1:10 anamuukitsa mwana wake wa mwamuna
1 Akorinto 6:14 Mulungu anamuukitsa Ambuye
15:15 Mulungu anamuukitsa Khristu.

#20) YESU ANAFA, MULUNGU SANGAFE. Yesu amamva njala ndi ludzu **Mateyu 4:2, Yohane 19:28** ndipo amatopa, **Yohane 4:6**. Anayesedwa **Mateyu 4:1** Anabvutika **Luka 24:26** Anafa **Yohane 19:33, 1 Akorinto 15:3,** Mulungu sangafe Iye ndi Mfumu yosapheka **1 Timotiyo 1:17, 6:15-16.**

#21) MWANA WA MWAMUNA AMALANDIRA MOYO KUCHOKERA KWA ATATE, ATATE NDI CHIYAMBI CHA MOYO. **Yohane 5:26** *popeza monga Atate ali ndi moyo mwa iye yekha; kotero anapereka kwa Mwana Wa Mwamuna kukhala ndi moyo mwa iye yekha*
Luka 1:35 Yohane 6:57 *Ndimakhala ndi moyo mwa atate.*

#22) MWAMUNA YESU NDI MTETEZI PAKATI PA MULUNGU NDI MWAMUNA.
1 Timoteo 2:5 *pali Mulungu mmodzi ndi Mtetezi mmodzi* ***pakati*** *pa Mulungu ndi Mwamuma, mwamuna Yesu.* **Agalatiya 3:20** Mtetezi Sali wa Mmodzi, koma Mulungu ali Mmodzi. Mtetezi ndi gawo la chitatu pakati pa okangana awiri.

#23) MULUNGU ANAMKWEZETSA YESU, Yesu sangakhale Mulungu chifukwa mwamuna amene adzikweza yekha adzatsitsidwa. **Afilipo 2:9** *Mwa ichinso Mulungu anamkwezetsa kwambiri* **Machitidwe 2:33,5:31** *Iye anakwezedwa*

ndi Mulungu **Mateyu 23:12, Luka 14:11,18:14** *wina aliyense wodzikweza yekha adzatsitsidwa*;

#24) YESU ANADZODZEDWA NDI KUPANGIDWA AMBUYE NDI MULUNGU. Atate wake anampatsa iye ulamuliro wake **Luka 1:31-33, Yohane 5:22,27, Machitidwe 2:36,10:38,42 17:31** *Mulungu anamupanga Yesu yemweyu Ambuye ndi Khristu*.

#25) MWANA WAMWAMUNA WA MULUNGU SALI WOYIMA PAYEKHA, MULUNGU NDI WOYIMA PAYEKHA. Mu **Yohane 5:17** yesu ananyozedwa ndi ayuda pogwira ntchito za sabata chifukwa anachiritsa pa sabata. Yakho lake kwa iyo likupezeka mu vesi **17:** *koma Yesu anayakha iwo Atate wanga amagwira ntchito kufikira tsopano, inenso ndigwira ntchito*. Tsopano ili silinali yakho lokhutira kwa iwo, linawapangitsa iwo kukwiya kwambiri, chifukwa mmalo mwa kutsika kukumvetsetsa
Kwa umodzi, anawazindikiritsa iwo adziwe kuti anali Atate amene anagwira ntchito. **18** *chifukwa cha ichi Ayuda anaonjeza kufuna kumupha iye, sichifukwa cha kuswa dzuwa la sabata lokha, komatu amachansokuti Mulungu ndi Atate wake; nadziyesera wofanana ndi Mulungu.* **19** *Ndipo Yesu anayakha ndi kunena kwa iwo, Indetu, Indetu, Ndinena kwa inu, Mwana wawamuna sangachite kanthu pa Iye Yekha, koma chimene waona atate akuchita: pakuti zimene iye azichita, zomwezo mwana azichita momwemo.*

Tsopano, Yesu akuuza Ayuda kuti Iye sangachite kanthu pokhapokha Atate amuonetse iye chochita. Iye akunena kuti Mwana wa Mwamuna SANGACHITE KANTHU, ndipo mwana wa Mwamuna sangapulumutse, iye sangachiritse, iye sangaombole,iye sangachite kanthu pokhapokha ataonetsedwa ndi atate chochita.

Awa si mau a Mmodzi amene ali Woyima payekha. Koma Mulungu ali Woyima payekha. Mulungu ndi wodziwa zonse ndi wamkulukulu.

1. Mmodzi amene ali woyima payekha sayakha kwa wina aliyense.
2 Mmodzi amene ali woyima payekha amalamulira mwa mphabvu kuposa onse.
3 Mmodzi amene ali woyima payekha ndi waufulu kwathuthu kwa ena onse.

Kotero, Mwana wa Mwamuna wa Mulungu sali Woyima Payekha, Iye amadalira kwathuthu pa Atate kuti achite ndi kulankhula. Iye analibe mawu akeake, ntchito kapena chiphunzitso, ndipo anapereka chifuniro Chake Chomwe kwa Atate.

Anali Mulungu amene anakhala mwa Mwana wa Mwamuna amene anali woyima payekha. Mulungu ndi wodziwa zonse ndipo Mulungu ndi wamkulukulu, koma Mwana wa Mwamuna amadalira pa Atate pa zinthu zonse kuonjezera; kulankhula,

kuchita, chiphunzitso chake, ndi kupereka chifuniro chake chomwe ku chifuniro cha Atate wake.

Mulozo wa Malemba	**Machitidwe a Woyima Payekha**	**Woyima Payekha**	**Woyima Payekha**
		INDE	**AYI**
Yohane 5:19 Mwana wa Mwamuna sangachite kanthu koma chimene Atate amuonetsa Iye	Sayankha kwa wina ali yense		**X**
Yohane 5:17 Atate wanga amagwira ntchito kufikira tsopano, Inenso ndigwira ntchito	Alamulira pamwamba pa onse		**X**
Yohane 7:16 Chiphunzitso changa sichanga koma cha Iye amene ananditumа	Waufulu kwathunthu		**X**
Yohane 14:10 Mau amene Ine ndilankhula ne sindilankhula za Ine ndekha, Atate amen akhala mwa Ine amachita ntchito			**X**
Aheberi 5:8 Ngakhale Iye anali mwana wa Mwamuna anaphunzira kumvera			**X**

Nanga bwanji za "*Atate, ngati nkutheka, chikho ichi chindipitirire Ine, koma simonga ndifuna Ine, koma Inu"*, ndi zina zotero. Awa si Mau a mmodzi amene ali woyima payekha. Malemba onse wolankhula za mwana wa mwamuna akusonyeza kuti iye sali woyina payekha.

Yohane 5:20 *Pakuti atate anakonda mwana wa mwamuna, ndi kumusonyeza zinthu zonse zimene amachita yekha: ndipo adzamusonyeza ntchito zazikulu zoposa izi, kuti mukaziwe.* Taonani kuti Yesu amadalira pa Mulungu kumusonyeza Iye masomphenya akuti achite Iye asanachite.
Yohane 5:21 *Monga Atate aukitsa akufa, nawapatsa moyo: momwemonso Mwana wa Mwamuna apatsa moyo iwo amene* [Atate] *afuna.*
Yohane 5:22 *Monga atate saweruza munthu aliyense, koma* ***anapereka*** [kumpatsa*] kuweruza konse kwa Mwana wa Mwamuna.*

Aroma 15:5 11 *Tsopano Mulungu wa chipiriro ndi chithondozo <u>apatse</u> inu kuti mukhale ndi malingaliro amodzi wina ndi mzake monga mwa Yesu Khritsu:*
Yohane 12:44 ***11*** *Yesu analira ndi kuti, Iye wokhulupirira ine, sakhulupirira ine <u>koma iye</u> <u>wondituma ine</u>.*
Yohane 5:23 *Kuti amuna onse alemekeze mwana wa mwamuna, <u>monganso</u> alemekeza Atate.* Iye *wosalemekeza Mwana wa Mwamuna salemekeza Atate amene anamtuma Iye*. Mu kulemekeza Mwana wa Mwamuna tikulemekeza Atate, chifukwa Mwana wa Mwamuna akuchita chimene Atate wa mulangiza Iye kuchita. Kotero chimene tikuona chikuchitika ndi Atate akugwira ntchito ndi momwemonse Mwana wa Mwamuna akugwira ntchito. Motero popereka Ulemu kwa Mwana wa Mwamuna tikubvomereza ukulu wa Atate, ndi udindo wathuthu wakumvera wa Mwana wa Mwamuna kwa Mulungu.

Yohane 5:24 *Indetu, indetu, ndinena kwa inu, Iye amene amva mau anga, ndi kukhulupirira pa **Iye ananditumа Ine**, ali ndi moyo wosatha, ndipo salowa mkuweruz; koma wachokera ku imfa nalowa mmoyo.*
Yohane 14:10b *Mau amene Ine ndinena kwa inu Sindilakhula kwa ine ndekha; koma **Atate wokhala mwa ine** achita ntchito zake.*

A Milungu Itatu amagwiritsa mikangano yambiri kuyetsetsa kufotokoza mmene Mulungu ndi Yesu aliri mmodzi monga chala chanu chiri chimodzi. Aumodzi kapena a Yesu yekha achitanso chimodzimodzi, koma mwa njira zosiyana. Motero A Milungu Itatu amaona pafupifupi kukhuza anthu awiri, iwo ayetsetsa kuwapanga kuti akhale mmodzi monga chinthu cha magawo atatu. Koma ife tasonyeza kuti sali mmodzi mwa njira imeneyo. Iwo ndi mmodzi mwa mau. Mulungu ndi Mau, ndipo Mau amenewo anaonetseredwa mwa munthu wa Mwana wake wa Mwamuna. Malemba otsatirawa ndi omwe a Milungu Itatu amagwiritsa ntchito kuyetsetsa kufotokoza zaumulungu wa Itatu.
Afilipi 2:6 *Pokhala nawo maonekedwe a Mulungu*
Akolose 1:15 *Fanizo la Mulungu wosaonekayo*
2 akorinto 4:4 *Khristu, amene ali chithunzithunzi cha Mulungu*
Yohane 12:45 *Iye amene waona Ine waona Iye*
Yohane 14:9 *iye amene Waona ine waona Atate*
Akolose 1:19 *Mwa iye chidzalo chonse chikhalira*
Akolose 2:9 *Mwa iye chikhalira chidzalo chonse*
Aheberi 1:3 *Pokhala chinyezimiro cha umunthu wake*

Malemba awa akhoza kuyikidwa mmagulu awiri a mikangano. Choyamba, amakhulupirira kuti Yesu anali mgawo la Mulungu kutanthauza kuti iye ndi

Mulungu. Iwo amakhulupirira motero chifukwa samamvetsetsa moyo wa - Mulungu.
Baibulo limaphunzitsa kuti Mulungu anaika thupi lathuthu mmimba mwa mkazi **Aheberi 10:5** *Thupi munandikonzera ine* [ndiko kuti: zonse dzira ndi umuna] **aheberi 1:3** limatiuza kuti mwamuna Yesu [thupi, Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] anabadwa ndi machitidwe onse ndi chikhalidwe chimene chinali mwa Mulungu. Mwa mau ena, Mulungu anatsanulira moyo wodzodza [DNA] mwa kunena kwina, [zonse zimene iye anali zinathiridwa njira ya moyo ya Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] ndipo kotero Thupi limenero linali chopumira cha moyo cha Atate, koma sichinali Atate, koma mu chifanizo cha Atate. Ndipo ngati ndi chifanizo chake si Atate iye mwini. Kotero ichi sichikusonyeza ngakhale mphindi imodzi kuti Yesu ndi Mulungu iye mwini. Mau akuti “chifanizo” likutanthauza *kufanana kapena chikhalidwe chogwirika*. Yesu anali chionetsero cha thupi cha moyo wa Mulungu mwa Mwamuna. Chikhalidwe chake chinawonetsera zonse zimene ziri Mulungu kapena moyo wa Mulungu uwawonetseredwa nthupi la munthu. Kotero amuna amadziwa chikhalidwe cha Mulungu kapena chifanizo chinali motani poona moyo wa Yesu. Moyo wake unawulula chiyero, chiyeretso, chilungamo, Chikondi, chifundo, kukonda-mofatsa, choonadi, kudzichepetsa, ndi kukhulupirika. Yesu sanali Mulungu Iye mwini; Iye amaonetsera khalidwe la Mulungu mwa moyo Wake wangwiro.

Malemba awa amene akulozera ku chidzalo chonse cha Umulungu mthupi kapena nkukhala mwa Khristu sizikumpangitsa Munthu kukhala Mulungu. Mulungu ndi Mzimu. Iyeyu si mnofu ndi mafupa. Koma Mulungu wosawoneka anadza pansi anakhala mwa Mwana wake pa Mtsinje wa Yorodano pamene Yohane anaona kuwala kwathunthu, (ndiye Chipilala cha Moto) Chikutsika pansi ndi kuwala pa Yesu ndi kukhazikika mwa iye. Kudzodza komweko kunamukokera iye mmunda mwa Getsemani. Mchifukwa chake analira pa mtanda kwa Mulungu wake, “Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwandisiyiranji ine. Kudzodza kunamchokera iye kotero anayenera kufa ndi imfa ya mthupi, chifukwa mmene monsemo Mulungu anamdzadza iye mu chidzalo chonse sakanafa ngakhale anayesa nthawi zambiri ndi njira zochuluka kuti athane naye.

Njira imodzi imene a Milungu Itatu amagwiritsa ntchito kunena kuti Yesu ndi Mulungu ndi malemba ochepa amene amatenga mu kuchokera ku nkhani.

Yohane 20:28 Lemba iti limatiuza za Tomasi amene anali wokaika ndipo mau amene wokaika uyu amene analankhula pamene anaona ndi kukhuza nthupi la Yesu. Taonani kuti Tomasi sanali ndi amnzake pamene Yesu anaonekera koyamba kwa iwo. Mu **Luka 24:29** tinaona nkhani yomweyo kumbvumbuluka tsopano,

Mulungu ndi Mzimu, koma Yesu anali mwamuna mmene mzimu wopambana waukulu umakhala. Atawapatsa moni, Yesu anawauza iwo "***monga Atate ananditumа ine kotero Ine nditumа inu***." Kusonyeza kuti iye sanali Atate, koma anatumizidwa ndi Atate, ndikotero mu kumvera kwa Atate. Tsopano popeza a Milungu Itatu amagwiritsa ntchito mau a Tomasi ngati umboni kuti Yesu anali Mulungu, ndiye satana ngokakamizidwa kugwiritsa ntchito mau a Farisi kuti Yesu anali wa mwano, chifukwa onse akhoza kupezeka mmalemba kulankhula za mmene iwo amakhulupirira chimene Yesu ali. Mkangano umenewu siungathe kuyima mayeso ambirimbiri a umboni wa Malemba amene ife tapereka. Popeza munthu wina anena mau ena mu Bible sizipangitsa mau amenewo Mau a Mulungu. Baibulo limati Yudasi anachoka ndi kudzipachika yekha, ndipo mu Lemba lina tikupeza Yesu akuti mu **Luka 10:37** "***Pita, nuchite iwe momwemo***." Inu muyenera kugawa mau a choonadi moyenera. Kugalukira kolakwika kwa mau kumabweretsa imfa yauzimu.

Lemba lina limene a Milungu Itatu amagwiritsa ntchito ndi **Tito 2:13** *Ndi maonekedwe a ulemerero wa Mulungu wamkulu ndi mpulumutsi wathu Yesu Khristu*; komatu lemba ili silikunena za Mwana wa Mwamuna wa Mulungu, koma za Atate wa ulemerero monga Paulo akulakhula za kubwera Kwake mu **Aefeso 1:17** ndi **1 Atesalonika 4:15-18**. Za kuonekera kulankhula za kupezekapo kwake kwa Mzimu Woyera [Mulungu iye mwini] Ambuye Yesu Khritsu asanafike kwenikweni mnthupi. Padzakhala kuonekera kwa atate wa Ulemerero pano pa dziko lapansi tisanapite kukakomana ndi Mwana wa Mwamuna wa Mulungu mlengalenga [osakhala pano pa dziko] monga ziriri mu Genesis, tikuona Mulungu akuonekera kwa mneneri Wake Abraham asanafike mwana wa lonjezano.

Lemba lomaliza limene limagwiritsidwa ntchito ndi a Milungu Itatu ndi **KJV Aheberi 1:8** *Koma <u>ponena</u> za Mwana wa Mwamuna iye anati, mpando wachifumu wanu, O mulungu, ufikira nthawi za nthawi: ndipo ndodo ya chifumu yoongoka ya chilungamo ndiyo ndodo ya ufumu wanu*. Tsopano kuwerenga mosamala kwa mau a chi giriki kukusonyeza cholakwa mu kutanthauzira liu la chi giriki "***PROS***" limatanthauzidwa ngati "***ponena"***, chimene chikunena kupita mnjira ya kwa ***Mwana wa Mwamuna wa Mulungu*** ndipo osakhala kuchokera kwa Mwana wa Mwamuna wa Mulungu, potero kuoneka ngati mau a iwo ochokera kwa Mulungu kwa Mwana wa Mwamuna ndipo osati kuchokera kwa Mwana wa Mwamuna kwa Mulungu Atate wake monga mmmene zinalembedwa kwenikweni ndi mtumwi Paulo, liu loyenera kwambiri mu chizungu ndi "***moyenera ndi"*** kapena "***mogwirizana ndi***" kotero nkhani iyenera kuwerengedwa moyenera, **Aheberi 1:8** *koma <u>**moyenera ndi**</u> Mwana wa Mwamuna Iye* [Mwana wa Mwamuna] *anati,*

Mpando wa chifumu, O mulungu, ufukira nthawi za nthawi: ndipo ndodo ya chifumu yoongoka ya chilungamo ya chilungamo ndiyo ndodo ya ufumu wanu. Ndipo Atate alankhulanso kwa iye mobwezera mu mzere wa lemba lotsatira. **9** *Mwakonda chilungamo, ndi kudana nacho choipa*; ***mwa ichi Mulungu, ngakhale Mulungu wanu,*** *wakudzodzani ndi mafuta a chikondwerero chenicheni koposa amnzanu.* Kudzodza uku ndi Mulungu kwa Mwana Wake wa Mwamuna kumene kwa lankhulidwa pano kwaonetseredwa mmalemba ena ambiri. Ndipo pomaliza tikuona mwana wa mwamuna akulankhula mobwezera kwa Atate wake, **10** *Ndipo Inu, Ambuye pachiyambipo munayika maziko ake a dziko, ndipo miyamba iri ntchito ya manja anu:* kotere tikuona kuti uku ndi kukambirana pa chiyambi cha bukhu la **Aheberi chaputa 1.**

Aheberi 1:1 11 *Mulungu, mu nthawi za kale amalankhula ndi makolo mwa aneneri mmanenedwe ambiri ndi mosiyana siyana,* **2** *Wachita mmasiku ano otsiriza kulankhula kwa ife mwa Mwana wa Mwamuna, mmeneIye* [Mulungu] *anamuika wolowa mnyumba wa zonse, mwa iyenso* [Mulungu] *analenga maiko*; **3 Ameneyo** [Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] ***pokhala chinyezimiro cha ulemerero Wake*** (wa Mulungu), ***ndi chizindikiro chenicheni cha chikhalidwe chake***, [cha Mulungu] *ndi kunyamula zonse ndi mau amphabvu yake* [ya Mulungu], *mmene iye* [Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] *adachita chiyeretso cha zoipa*, [Iye, Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] *amakhala pa dzanja la manja la ukulu mmwamba;* [wa Mulungu] **4** *Atapangidwa kukhala wabwino kuposa angelo, monga* ***Iye*** [Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] ***adalowa dzina lopambana lakuposa iwo***. [Kotelo ngati Iye anapeza dzina lake mwa kulowa, ndiye kuti poyamba analibe, koma anapatsidwa dzina limeneli, ndi Atate wake.] **5** *Pakuti kwa angelo uti anati* [Mulungu] *nthawi iliyonse, Iwe ndiwe Mwana wanga wa Mwamuna, lero Ine ndakubala iwe? Ndiponso, Ine* [Mulungu] *ndidzakhala kwa Iye* [Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] *Atate, ndipo Iye* [Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] *adzakhala kwa Ine Mwana wa Mwamuna*? **6** *Ndiponso pamene Iye* [Mulungu*] atenganso woyamba wobadwa* [Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] *kulowa naye mdziko,Iye* [Mulungu] *anena, ndipo amgwadira iye* [Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] *angelo onse a Mulungu***. 7** *Ndipo kwa angelo Iye* [Mulungu] *anenadi, Amene apanga mizimu ya angelo ake* [a Mulungu] *lawi la moto*. **8** *Koma molingana ndi Mwana wa Mwamuna wa Mulungu* iye [Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] *ati, mpando wa chifumu wanu, O Mulungu, ufikira nthawi za nthawi: ndipo ndodo ya chifumu yoongoka ndiyo ndodo ya ufumu wanu,* **9** *mwakonda chilungamo, ndi kudana ancho choipa; kotero Mulungu, ngakhale Mulungu wanu,* [Mulungu wandani? Mulungu wa Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] *wakudzodzani inu*

[Mwana wa Mwamuna wa Mulungu] *ndi mafuta a chikondwerero chenicheni kuposa amnzanu* [a Mwana wa Mwamuna a Mulungu].

Nkutanthauzira mu **NIV** timawerenga **Aheberi 1:3** motere: "Mwana wa Mwamuna ndi chionetsero cha ***ulemerero wa Mulungu*** ndi ***choyimira chenicheni cha umunthu wake***, kusamalira zinthu zonse mwa mau ake a mphabvu."

Timaonanso mu kutanthauzira mu **Amplified** za **Aheberi 1:3** " *Iye ndi chionetsero chokhacho cha ulemerero wa Mulungu, -chokhacho cha kuwala,-chionetsero cha uzimu. Ndipo iye ndi chosindiza cha ngwiro ndipo chifanizo chenicheni cha chikhalidwe cha Mulungu, kusunga, ndi kusamalira ndi kutsogolera ndi kuongolera za mwamba ndi mau ake Aukulu Amphabvu*."

Kuthandauzira kwina kuli konse kwa uku kungaulutse motsutsana ndi choonadi cha lemba ndipo Mau a Yesu Khristu Iye mwini mu **Yohane 17:3** *Ndipo uwu ndi moyo wa muyaya,* ***kuti iwo adziwe inu Mulungu yekhayo woona****, ndi Yesu Khristu, amene inu mwamtuma*.

Mu Chipangano chakale Mulungu amadziwika ngati Mulungu Woona Mmodzi. **Yeremiya 10:10** *koma AMBUYE ndi Mulungu woona, Iye ndi Mulungu wamoyo, ndi mfumu yosatha*:

Komanso iye walankhulidwanso ngati Mulungu woona mu **2 Mbiri 15:3** *Tsopano papita nyengo yayitali Israel anakhala wopanda Mulungu woonayo, ndi wopanda wansembe wakuphunzitsa, ndi wopanda chilamulo.*

Mu kutseka a Umodzi kapena a Yesu yekha amagwitsa ntchito Malemba otsatirawa akupezeka mu 1 Yohane 5:20 ngati chitsimikizo chawo chakuti Yesu ndi Mulungu. "N*dipo tidziwa kuti* ***Mwana wa Mwamuna wa Mulungu wafika****, ndi* ***kutipatsa ife chidziwitso, kuti tinzindikire iye amene ali woona****, ndipo ife tiri mwa Iye amene ali woona, ngakhale mwa Mwana wake wa Mwamuna Yesu Khristu. Uyu ndi Mulungu woona, ndi moyo wamuyaya."*

Tsopano, iwo amawerenga awa ngati tiri mwa Mulungu mmodzi woona amene ali Yesu Khristu. Koma ngakhale mau amagwiritsidwa ntchito ndipo amathandauza njira yomweyo, ndiye lemba ili liyenera kuwerengedwe motere. *Ndipo ife tikudziwa kuti* ***Mwana wa Mwamuna wa Mulungu wabwera,*** *ndipo* ***watipatsa ife Kumvetsetsa, kuti timdziwe Iye amene ali woona Mulungu Yekhayo Woona****, ndipo* ***ife tiri mwa Iye amene ali Woona, mwanjira yomweyo monga*** *Yesu Khristu Mwana wake wa Mwamuna ali mwa Iye.* Icho ndi chimene Yesu anapemphera kwa Atate mu **Yohane 17** *Kuti ife tikhale mmodzi monganso Iye ndi Atate wake anali mmodzi.*

William Branham Mneneri wa Mulungu ku mbadyo uwu wotsiriza anatsindika ubale pakati pa Mulungu, ndi Mwana wake wa Mwamuna Yesu Khristu ndi mau otsatirawa.

Kuomboledwa Kwathunthu 59-0712 P.55 *Yesu anali yense, Mwamuna weni weni. Iye akanatha kulira ngati mwamuna, Iye akanatha kudya ngati mwamuna; Iye akanatha kuchita ngati mwamuna. Iye anali yense, mwamuna weni weni mthupi lake lanyama. Ndipo mu Mzimu Wake, anali Yense, Mulungu weni weni, kotero* ***anapanga thupi Lake kugonjera ku Mzimu umene unali mwa Iye****. Mukuona inu, Iye anayesedwa mu mmakhalidwe onse monga ife. Iye anali Mwamuna, osakhala Mngelo. Iye anali Mwamuna. Iye anali ndi zikhumbokhumbo ndi mayesero monga ife timachitira. Baibulo limati Iye amachita. Iye Mwamuna, osakhala Mngelo amene ali pamwamba pamayesero.* **Aheberi 1:4** *kuti anapangidwa wocheperapo kusiyana ndi Angelo. Iye anali Mwamuna, Mwamuna wathunthu, ndi kuti Mulungu anatenga Mwamuna wathunthu kuti abweretse kuomboledwa kwathunthu;* ***ndipo Iye anamudzadza Iye ndi Mzimu Wake; Mzimu Woyera unali mwa Iye wopanda Muyeso.*** *Ndipo Iye anayesedwa monganso ife. Ndipo Iye anali Mulungu wathunthu. Iye anatsimikizira ichi pamene Iye anadzutsa akufa, pamene anayimitsa chilengedwe, Nyanja yobuma ndi mphepo yayikulu. Pamene analankhula ku mitengo, ndi zotero, Izo zinamvera Iye. Iye anali Mulungu mkati. Ndipo Iyeyu anakhala Mwamuna, pakuti* ***Iye anali Mwamuna, koma Iye anadzipereka kwathunthu ngati Mwamuna mmanja mwa Mulungu kuutumiki wa Mulungu****. Ndipo Iye ndi chitsanzo chathu.*

<u>TIONETSENI IFE ATATE ZITIKWANIRITSA 56-0422 E-36</u>

Tsopano, ndi nthawi zambiri zikunenedwa kuti palibe mwamuna angathe kuona Mulungu nthawi yina ili yonse, Baibulo linanena choncho. Koma yekhayo wotengedwa wa Atate anamulengeza Iye. Filipo, pano anali wofunitsitsa; iye adafuna kuona Atate. Akunena pano iye anati, "Ndakhala ndi Iwe nthawi yayitali, Filipo, ndipo sundidziwa Ine?' anati, pamene uona ine waona Atate Wanga." ***Mu mau ena, uona Atate akudziwonetsera yekha kudzera mwa Mwana wa Mwamuna. Iye ndi Atate anali mmodzi mu ganizo lakuti Atate wake amakhala mwa Iye, osakhala Iye kuchita ntchito; Iye anali mwana wa mwamuna, iye mwini,*** *wathupi, wobadwa mwa unamwali, Mwana wa Mwamuna wa Mulungu. Ndipo* ***mwa Iye mumakhala Mulungu Atate, kudziwonetsera Iye mwini ku dziko****, mchitidwe wake kwa anthu. Mukuona? Chabwino, ndi* ***mmene Khristu ndi Mulungu analiri mmodzi****.* ***Mulungu anali <u>mwa</u> Khristu*** *kuyanjanitsa dziko kwa Iye Mwini. Tsopano, Iye anati, "Pamene muona Ine, mwaona Atate, ndipo chifukwa chiyani mukunena kuti, 'Tionetseni Ife atate?*